# CHIDULE CHA ZOKAMBIRANA CHA MISOKHANO YA ANTHU OKHUZIDWA YOMWE INACHITIKA 14TH April 2025 AND 17TH APRIL 2025

## CHIYAMBI

Kampani ya Effective Climate Solutions 1 FZCO ("ECS") yomwe ndi bungwe lolumikiza ndi kuyang'anira (CME) zochitika za pulojeketi ya mbaula za Ecoa mogwirizana ndi ECOA Climate Capital (ECC) omwe akuyendetsa pulojekiti iyi akuitana onse okhuzidwa  kuti awunike zotsatira za zokambirana zomwe zinachitika ku misokhano ya anthu okhuzidwa yomwe inachitika  kuyambira pa 14 mpaka 17 April 2025 ku Lilongwe ndi Blantyre, Malawi. Panthawi ya misonkhano imeneyi, Effective Climate Solutions 1 FZCO ("ECCS1") ndi mabungwe ogwirizana nayo anabweretsa pulojeketi ya kuphika kwa makono ndi mwaukhondo yomwe ndi yogawa mbaula m'dziko la Malawi. Ntchito za mu Pulojekiti iyi (VPAs) zili pansi pa zochitika za Gold Standard (PoA); Njira Zabwino Zophikira Pogwiritsa Ntchito Nkhuni/Makala mu Africa"

## ZOLEMBEDWA ZA MISONKHANO:

### Kalembela:

Oitanidwa atafika anauzidwa kuti alembetse maina mukalembera wa msokhano. Anthu omwe anatenga nawo mbali podzera pa zoom analembetsa pomwe amalowa mu msokhano.

### Mawu Oyambirira:

Anthu oitanidwa analandilidwa ndi ogwira ntchito ku Eco Climate Solutions mu misokhano yonse. Kudziwana kunachitika kwa anthu omwe anafika ku msokhano komanso kwa amene anatenga nawo mbali pa zoom. Cholinga cha msokhano chinakambidwa kwa anthu omwe anafika.

### Chiwonetsero Cha Pulojeketi:

Ogwira ntchito ku ECC anayambitsa msokhano ndipo anawafotokozera mwatsatane tsatane mmene pulojeketi ingayendere. Anakambanso  kuti kampani ya Effective Climate Solutions 1 FZCO ("ECS") ndi yomwe ikuyang'anira zochitika za pulojeketi mogwirizana ndi kampani ya ECOA Climate capital (ECC) ngati yomwe ikuyendetsa ntchito za pulojeketi, cholinga cha pulogalamu ndi ubwino wake ubwino kwa anthu m'mdera,  komanso za ukadaulo womwe waikidwa mu mbaula zimenezi.

Anatenganso nthawi kukumbutsa oitanidwa za kusitha kwa nyengo ndi zotsatira zake.  Anafotokonzanso mwachidule za thandizo lomwe limabwera posamala chilengedwe, m'mene thandizoli limabwerera, ndiponso m'mene pulojeketi imachitira kuti ipeze thandizoli. Ogwira ntchito ku ECC anafotokonzanso mwatsatane kwa onse okhuzidwa m'mene umwini wa nthandizo lobwera posamala chilengedwe limapitira ku kampaniyi . Anawasonyeza za ka ulusi komwe kamakhala pa mbaula komwe kamadulidwa  kuvomereza kuti umwini wa

thandizoli lapita ku kampaniyi. Cholinga chotengera umwini wa thandizoli chinafotokozeredwa komanso m'mene thandizoli limagwirira ntchito. .

**Nthawi ya Mafunso ndi Mayakho:**

Okhuzidwa nafunsa mafunso patatha kufotokoza za pulojeketi imeneyi. Anafunsa za ubale umene uli pakati pa kampani ya ECC and ECO, mtengo ndi upangiri wa mbaula zamakono zimenezi, nthawi yomwe pulojeketi igwire ntchito zake, ndi ndondomeko za m'mene mbaulazi zingagawidwire. Anasonyezanso chidwi pa zochitika za pulojeketiyi, makamaka amayi. Oitanidwa anatsindikanso zaubwino wowonetsetsa kuti mbaulazi zikupezeka ku madera akumudzi pa mtengo wosaboola mthumba, komanso kuganizira amayi omwe ali mu magulu kupeza mbaula zimenezi polipira mwa pang'ono pang'ono Mafunso onse ndi ndemanga zawo zinayakhidwa bwino ndi mogwira mtima.

**Chiwonetsero cha Mfundo Zoteteza ndi Kafukufuku wa Kukhazikika mu Pulojekitiyi**

Ogwira ntchito ku ECC anafotokonzanso za mfundo zoteteza zomwe zimatsatidwa komanso m'mene angazachitire kawuniwuni wa mfundo zimenezi. Okhuzidwa anauzidwanso kuti pali mwayi wopitiriza a kupereka ndemanga zawo, komanso kukambirana pa zochitika za pulogalamuyi kudzera ku ofesi yawo. Msokhano unapitiliranso ndi kuwafotokozera za mfundo zachitukuko zokhazikika ndi m'mene pulojeketi imeneyi ithandizire kulimbikitsa zina za mfundo zimenezi. Okhuzidwa anakhutisidwa ndi kuwunikira kwa mfundo zimenezi ndipo panalibe mafunso ena ali wonse. Ogwira ntchito ku ECC anakambanso za m'mene madando okhuza ntchito za pulojeketi aziperekeredwa ndi m'mene aziwunikira mfundo za chitukuko zokhazikika zimenezi.

**Kutseka Msokhano:**

Ma pepala owunikira m'mene msokhano unayendera nagawidwa kwa onse oitanidwa. Anthu anakhutisidwa ndi m'mene msokhano unayendera ndipo anapeleka ndemanga zabwino. Polamiza penipeni pa msokhano panali chionetsero cha mbaula zogwiritsa ntchito makala ya Ecoa.

**NDEMANGA ZOBWERA PA MSOKHANO KUCHOKERA KWA ANTHU OKHUZIDWA**

| Wokhuzidwa wa Mwamuna/ Mkazi | Ndemanga ya Okhuzidwa | Kodi ndemanga inatengedwa? (Eya/ Ayi)? | Kufutokoza (Chifukwa? Bwanji?) |
|---|---|---|---|
| M | Kodi ECC imalimbikitsa | Eya | ECC imapanga mbaula za mitundu zosiyana siyana zomwe |

| Wokhuzidwa wa Mwamuna/ Mkazi | Ndemanga ya Okhuzidwa | Kodi ndemanga inatengedwa? (Eya/ Ayi)? | Kufutokoza (Chifukwa? Bwanji?) |
|---|---|---|---|
| | abizinesi komanso mabungwe kuti atenge nawo mbali mu pulojeketi imeneyi? | | zingagwiritsidwe ntchito mu malo a bisinesi komanso mabungwe monga m’sukulu. Koma panopa chidwi chili pa mbaula zogwiritsa ntchito makala pakhomo. |
| M | Kodi mbaula zinaikidwa nambala yothandizira kuiwunikira | Eya | Mbaula ina iliyonse ili ndi nambala yake yothandizila kuiwunikira. Mbaula ikagulidwa, ogwiritsa ntchito amapereka dzina lake kuti ithandize kutsatira mbaula imeneyi. |
| F | Kodi mtengo wa mbaula ndi zingati? Kodi mtengowu ndi wotsika kwa anthu omwe aikidwa mu pulojeketi imeneyi kuti akwanitse kugwiritsa ntchito makomo mwawo? | Eya | Mtengo uzatsitsidwa kuti ogwiritsa ntchito athe kuipeza kudzera ku thandizo lomwe limabwera posamala chilengedwe. |
| F | Kodi mbaula zimagwiritsa ntchito makala aliwonse? | Eya | Mbaula za ECOA Char stove zimagwiritsa ntchito makala aliwonse omwe amapezeka m’dziko muno komanso ma briquettes. |
| M | Kodi mbaula za ECOA zimagwira ntchito kwa nthawi yaitali bwanji? Kodi zimasamalidwa mosavuta? | Eya | Mbaula za ECOA zimakhala zaka 7-9 zikugwira ntchito, komanso zimayendera ndi m’mene munthu kausamalira kuti zigwiri bwino ntchito yake. Mbaulazi zimasamalidwa mosavuta. Palinso malangizo omwe anaikidwa mu bukhu la kagwiritsidwe komwe kamakamba zambiri, komanso omwe amagulitsa mbaulazi amafotokoza za m’mene mbaulazi zingasamalidwei. |

| Wokhuzidwa wa Mwamuna/ Mkazi | Ndemanga ya Okhuzidwa | Kodi ndemanga inatengedwa? (Eya/ Ayi)? | Kufutokoza (Chifukwa? Bwanji?) |
|---|---|---|---|
| M | Kodi tingazindikire Bwanji mbaula ya chinyengo ya Jikokoa? | Eya | Mbaula zonse zimabwera mu bokosi yake ndi namabala yakeyake komanso bukhu lokamba chitsimikizo chakuti mbaula siyachinyengo. Mbaula zimapatsidwa chitsimikizo chakuti zitha kugwira bwino tchito kwa chaka, kuonjezera apo, mbaula zimagulutsidwa ndi anthu ovemerekezeka ndi kampaniyi. |
| M | Kodi pali upangili wakuti ECC ingagwire ntchito ndi boma komanso makampani ena kubweretsa mbaula zina zaukhondo kusiya za makalazi | Eya | ECC ili kuthekera kulumikizana ndi ma gawo oyenerera aboma komanso magulu ena pothandiza kubweretsa njira zaukhondo zophikira.<br><br>Pamene ili mu gulu la makampani obweretsa njira za bwino zophikira muno mu Malawi, ECC izakhala tcheru kuona upangiri uliwonse wolimbilitsa njira zina zabwino zophikira. |
| F | Kodi mbaula zizakhonzedwa Bwanji ndipo njie yake izakhala motani? | Eya | ECC izakhazikitsa malo okhonzera mbaula zigawo zonse za dziko lino. Izi zizabweretsa ntchito, Kuthandizira mfundo za chitukuko chokhazikika. Makomo omwe ali pa Kaundula azakhonzetsa mbaula zawo malinga ndi Chitsimikizo chomwe chaperekedwa pamene tikugula mbauala. |
| M | Kodi pali malingaliro okulitsa ntchitoyi ku madera ena omwe amagwiritsa ntchito nkhuni komanso makala. | Eya | Pulojeketi imeneyi ichitika magawo awiri a mdziko muno (Blantyre ndi Lilongwe). Mtsogolo muno ntchito zake zizafikira madera ena potengera chikonzero cha pulojeketi. |

| Wokhuzidwa wa Mwamuna/ Mkazi | Ndemanga ya Okhuzidwa | Kodi ndemanga inatengedwa? (Eya/ Ayi)? | Kufutokoza (Chifukwa? Bwanji?) |
|---|---|---|---|
| M | Kodi ndi ntchito zanji zomwe ECC zikugwira kuzindikiritsa anthu za kuipa kwa kusitha kwa nyengo | Yes | ECC & ECS imapereka unthenga ndi kuzindikiritsa anthu za zotsatira za kusitha kwa nyengo. Izi zimachitika kudzera ku maphunziro, kulengeza pa misokhano yonenelera malonda, misokhano ya athu okudzidwa, ndi ina yomwe anthu amapezeka. |
| F | Mbaula za ECOA zimagwiritsa ntchito makala zomwe zimathandiza kudula mitengo. Kodi pamenepa zikusiyan bwanji ndi zochitika zoononga chilengedwe? | Eya | Mbaula za ECOA zimagwiritsa ntchito makala ochepa okwanira theka la lomwe mbaula zachikale zingagwiritse ntchito. Komabe sikuti ndi njira yabwino kwambiri koma ndi chiyambi chopita chitsogolo popeza njira zadalilika zosiya kugwiritsa ntchito makala kapena nkhuni. Mbaulazi zimachepetsa utsi woipa woononga chilengedwe |
| M | Kupatula kugawa mbaula. Kodi BURN imathandiza anthu ndi njira zina zolimbikitsa kudzala mitengo, kuthandizila kuchepetsa kuwonongeka kwa chilengedwe? | Eya | ECC & ECS pakadali pano ikupanga zochitika zosunga mitengo zomwe anthu azauzidwa bwino lino. |
| F | Kodi mbaulazi zingakwanitse kuthandiza mabanja omwe muli anthu ambiri omwe amagwiritsa ntchito mapoto akulu? | Eya | Mbaula Ecoa zili ndi kuthekera kophikira anthu okwana 0–12; motero ndi zabwinonso kwa mabanja akulu. |
| M | Kodi kuyipa ndi ubwino wodziwika wa | Eya | Mbaula zimenezi zimasunga makala, kuchepetsa utsi woipa pamene tikuphikira m'nyumba |

| Wokhuzidwa wa Mwamuna/ Mkazi | Ndemanga ya Okhuzidwa | Kodi ndemanga inatengedwa? (Eya/ Ayi)? | Kufutokoza (Chifukwa? Bwanji?) |
|---|---|---|---|
| | mbaula za ECOA ndi wotani? | | komanso ndi zachangu pophikira.<br><br>Palibe kuyipa kulikonse kodziwika pa mbaulazi. |
| F | M'chifukwa chiyani tikufuna madera a kumudzi komanso m'mtauni okha? | Yes | Malingana ndi kafukufuku amene anachitika wa pulojeketi imeneyi, anaonetsa kuti malo amene amagwiritsa ntchito kwambiri makala ndi kumidzi ndi m'mtauni. Pofuna kuti ubwino wake uonekere bwino, ndi kwabwino kuti mbaulazi zipezeke madera amenewa. . |
| M | Kodi mwaika njira zotani kupewa kuwerenga kawiri kwa m'mene mbaula zikuchepetsera kuika utsi oipa m'makomo. | Eya | Panthawi yogawa mbaula, ogulitsa azapanga kafukufuku wa mitundu mbaula zamakono zomwe makaomo akugwiritsa ntchito. Ngati khomo lili ndi mbaula ya makono sizalandila mbaula ya ECOA. |
| F | Kodi ndi mlingo wanji Waikidwa popanga mbaula zimenezi? | Eya | Milingo iyi ndi yomwe yaikidwa popanga mbaula zimenezi:<br><br>ISO 19867-1:2018 — yoyeza kagwiridwe kake ka ntchito.<br><br>ISO 9001 — yoyeza chikhalidwe cha m'mene amapangira kufakitale.<br><br>ISO 14001 — yoyeza kutetezakwa chilengedwe pamene akupanga ku fakitale. |
| F | Kodi njira zanji zingaikidwe poyang'anira ndi kuwunikira kuti unthenga woyenera | Yes | ECC izagwiritsa ntchito akaswiri opereka uthenga kwa makasitomala ake poonetsetsa kuti mafunso kapena madandaulo akuyakhidwa mwansanga. |

| Wokhuzidwa wa Mwamuna/ Mkazi | Ndemanga ya Okhuzidwa | Kodi ndemanga inatengedwa? (Eya/ Ayi)? | Kufutokoza (Chifukwa? Bwanji?) |
|---|---|---|---|
| | ukupititsidwa ku makomo. | | |

**MFUNDO MWACHIDULE ZA KUTETEZA**

Pa msokhano panakambidwa kuti cholinga cha pulojeketi ndi kuwafotokozera anthu za mbaula za makono zomwe ndi za ukhondo komanso zimagwiritsa ntchito makala ochepa pakhomo. Motero, pulojeketi izabweretsa ubwino pa chikhalidwe, chuma, ndi chilengedwe. Njira izi zoteteza zinakambidwa mwatchutchu;

| Mfundo Yoteteza | Kuwunikira |
|---|---|
| Ufulu wa Chibadwidwe | Polojeketiyi imalemekeza ufulu wa chibadwidwe ovemelekezeka m’maiko onse ndipo simalekelera pa nkhani yopwanya ufulu wachibadwidwe kapena khanza za mtundu wina uliwonse motsatana ndi malumbiro a maiko olimbikitsa ufulu wachibadwidwe. Polojeketiyi sizachita tsankho kwa aliyense ndipo izapeleka mwayi woti aliyense atenge nawo mbali pa zochitika zake. |
| Kusasankhana pakati pa Amayi ndi Abambo ndi ufulu wa Amayi | Polojeketiyi sikuvomereza mchitidwe wina uliwonse osalana chifukwa chakuti ndi amayi kapena abambo. Polojeketiyi izaganizira ntchito komanso kuthekera kwa amayi ndi abambo potenga nawo mbali muziganizo kapena kupanga zochitika za m’polojeketi. Izaonetsetsa kuti magulu onse a amayi ndi abambo akuitanidwa ku mikumano/msonkhano wa anthu okhuzidwa mu polojeketiyi. |
| Umoyo wa M’mudzi, Chitetezo ndi Ufulu wa Ogwira Ntchito | Polojeketi sizapeleka chiopsezo chili chonse choononga moyo ku madera amene kuzachitike ntchito zake kapena kwa ogwira ntchito ake. |
| Mbiri ya Chikhalidwe, Mbadwa za M’dera, Kuthamangitsidwa kapena kusamutsidwa. | Polojeketiyi ilibe zotsatira zoyipa ku Mbiri ya Chikhalidwe, Mbadwa za M’dera, Kuthamangitsidwa kapena kusamutsidwa kwa anthu. |
| Ziphuphu | Polojeketiyi simatenga nawo mbali kapena kulimbikitsa ziphuphu pogwira ntchito zake. |
| Zotsatira za Chuma | Polojeketiyi izalemekeza ufulu wa anthu ogwira ntchito. Palibe zoyipa zimene zingabwere pa za chuma kudzera ku ntchito zake. Chomwe chikuyembekezeka ndi kuthandiza kukweza chuma chokhazikika. |

| | |
|---|---|
| Nyengo ndi Mphamvu Za Chilengedwe | Polojeketiyi ichepetsa utsi woipa omwe umaononga chilengedwe ndipo izaonetsetsa kuti zochitika zake zikukwaniritsa ndondomeko ya Carbon Standard. |
| Madzi | Polojeketiyi sizaonga madzi, kusokoneza m’mene madzi amayendera, komanso kupangitsa kukokoloka kwa nthaka. |
| Zachilengedwe, ndi kagwiritsidwe ka malo | Polojeketiyi ilibe kuyipa kulikonse poononga chilengedwe ndipo sizatenga malo kumapangira ulimi. Kutulutsa utsi woipa woononga chilengedwe kuzachepa kwambiri chifukwa chogwiritsa ntchito mbaula za makono. |

Kafukufuku anachitika movetsetsana komanso onse kutenga nawo mbali. Okhuzidwa nagwirizana ndi mmene kafukufuku nachitikira ndi kampani ya BURN.

**CHIDULE CHA KAFUKUFUKU WA MFUNDO ZA CHITUKUKO CHOKHAZIKIKA.**
Pulojeketi imeneyi izathandizira mfundo za chitukuko chokhazikika motere:

| **Mfundo ya Chitukuko Chokhazikika** | **Cholinga** | **Njira zowunikira Chizindikiro** |
|---|---|---|
|   o | 1.4 Kuwonetsetsa kuti abambo ndi amayi makamaka osauka ndi amene ali ndi mwayi ofanana pakapezedwe ka chuma ndi zinthu zina zofunika pa moyo wao monga; malo, katundu, luso la makono loyenera ndi chuma monga mwayi wa ngongole zing’onozing’ono pofika mchaka cha 2030. | Kusunga ndalama zomwe timagwiritsa ntchito pogula makala<br><br>Kupanga kafukufuku wa chikhalidwe cha anthu omwe akugwiritsa ntchito mbaula kuti tipeze ndalama zomwe akugwiritsira ntchito pogulira makala kusiyana ndi momwe zinariri pa chiyambi. |
|   | 3.9 Kuchepetsa imfa ndi matenda zomwe zimabwera chifukwa cha mankhwala owopsa ndi kuwonongeka kwa mpweya, madzi ndi nthaka pofika m’chaka cha 2030 | Kukhala ndi pweya wabwino<br><br>Kupanga kafukufuku wa chikhalidwe cha anthu omwe akugwiritsa ntchito mbaula kuti tipeze ngati pali zisikonezo zili zonse chifukwa chakuipitsidwa kwa mpweya (kuchuluka kwa utsi, kuyabwa kwa maso, komanso kuvutika popuma) kusiyana |

| **Mfundo ya Chitukuko Chokhazikika** | **Cholinga** | **Njira zowunikira Chizindikiro** |
|---|---|---|
| | | ndi momwe zinaliri pa chiyambi. |
|   | 4.3 Kuwonetsetsa kuti amayi ndi abambo akupeza mwayi wofanana komanso osavuta pamaphunziro apamwamba aluso la ntchito zamanja ndi sukulu za ukachenjede pofika mchaka 2030. | Chiwerengero cha anthu omwe alandira maphunziro a luso kuti azidalire pawokha. |
|   | 5.4Kuthetsa mchitidwe osala amayi ndi atsikana pena pali ponse. | Luso la mbaula zimenezi zizalora kuti kuphika kuzitenga nthawi yochepa komanso kugwiritsa ntchito makala ochepa. Izi zizapangitsa kuti amayi/ atsikana kukhala nthawi yopuma komanso ktenga nawo mbali pazochitika za mdera. |
|   | 7.1 Kuwonetsetsa kuti anthu onse akupeza magetsi odalirika, okhazikika, amakono ndi otsika mtengo pofika mchaka cha 2030.<br>7.B Kukuza ntchito zomangamanga ndi kukweza luso loperekera ntchito zamakono, zokhazikika zamagetsi ku maiko okwera kumene makamaka osauka potsatira ndondomeko zothandizira ntchito zamagetsi pofika mchaka 2030. | Chiwerengero cha mbaula za makono zomwe sagulitsidwa kapena zikugwiritsidwa ntchito. |
|   | 8.5Kupezetsa amayi, abambo, achinyamata ndi anthu aulumali | Chiwerengero cha ntchito zomwe zalembedwa |

| **Mfundo ya Chitukuko Chokhazikika** | **Cholinga** | **Njira zowunikira Chizindikiro** |
| --- | --- | --- |
| | ntchito zokhazikika, ndikuwonetsetsa kuti akulandira malipiro ofanana molingana ndi ntchito zimene akugwira pofika mchaka cha 2030 | |
|  | 13.3 Kulimbikitsa kuphunzitsa ndi kudziwitsa anthu ndi mabungwe kuti akhale ndi kuthekera kolimbana ndi ziopsyezo zomwe zimabwera chifukwa cha kusintha kwa nyengo. | Kuchepa kwa utsi woonjezera kutentha |
|  | 15.3 Kuthana ndi vuto la chipululu, kubwezeretsa nthaka yoguga kuphatikizapo malo amene apanga chipululu okhudzidwa ndi kusowa kwa mvula ndi madzi osefukira polimbikitsa kuthetsa kuwonongeka kwa nthaka padziko lonse pofika mchaka cha 2030. | **Reduction in firewood and charcoal.** Surveys and monitoring of firewood consumption trends in project households compared to baseline households to assess impact on forest resources. |

Kafukufuku wa chitukuko chokhazikika wunachitidwa ndi mogwirizana ndi kafukufuku wa ECC. Pokhudza kuwunika zizindikiro za chitukuko chokhazikika, anthu okhudzidwa analibe ndemanga zina kapena maganizo okhudza kuunika kwa zizindikiro za chitukuko chokhazikika. Anagwirizana kuti apitirize ndi zizindikiro zomwe zinasankhidwa ndi ECC.

**KULUMIKIZANA:**
Ngati mukufuna kutipeza kuti mudziwe zambiri, mungalumikizane nafe munjira izi;

| | **Njira Yosakhidwa** | **Cholinga chosakha ( njira yabwino)** |
| --- | --- | --- |
| | | |

| | | |
|---|---|---|
| **Kupereka maganizo/madando mu bukhu** | Burn Manufacturing Malawi Limited<br>4th Floor Unit 1 NBS Building, Corner Victoria Avenue, Chilembwe Road<br>P.O. Box 2039,Blantyre-Malawi | Okhuzidwa anali osangalala kuti buku la madando lizipezeka ku ofesi ya kumalawi. Maganizo/Madando awo aziwapereka mosavuta ku ofesi yayikulu ku Malawi. |
| **Gold Standard kontakiti** | help@goldstandard.org | Yoyenera malingana ndi mfundo za Gold Standard |
| **Telephoni** | +265 111 89 99 85 | Namabal ya phoni ya ofesi yakumalawi. |
| **Makina a Intaneti komanso imelo** | BURN: info@burnmfg.com<br>Customercare.ng@burnmfg.com | Imelo ya BURN's |